JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION

"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774
10101 Lusaka, Zambia

Tel: 260-1- 290410 **Fax: 260-1-290759**
E-mail: jctr@jestuits.org.za **Web: www.jctr.org.zm**

29 January, 2007

Moni!

Tikuyamba nyengo ya Lenti, nyengo ya masiku makumi anai (40) amapemphero, kudzimana ndi kugawana ndi osauka. Monga ngati Akhristu, pa nyengo ino, tikupemphedwa kusinkha-sinkha pa ucimo omwe tili nawo pa kulapa ndi kuyambanso umoyo wina pokonzekera caka cacikulu ca Pasaka.

Ndife okondwa kukutumizirani uthenga wathu wa nyengo ya lenti wa caka ca 2007. Tikhulupirira kuti njira ya ciKatolika yofalitsiramo uthenga wabwino pa zamkhalidwe wa anthu (Church Social Teaching) idzadzetsa phindu ku njira zina zofalitsiramo uthenga pa nyengo yodalitsika ino ya Lenti.Tizindikira kuti njirazi zidzafotokozedwa bwino ndi azitsogoleri a m'madera osiyana-siyana kulingana ndi zomwe akukumana nazo. Mutha kugwiritsa nchito njirazi pa mapemphero anu a padera, pa misonkhano ya pa mbumba, m'magulu ya acinyamata ndinso m'magulu amaphunziro (study groups).

Njira zofalitsiramo uthenga wa Lenti za caka cino ziyang'ana pa mbali zosiyana-siyana zomwe munthu angasinthiremo malo ake ndiponso dziko lake; kuonjezerapo, ziyang'nanso pa momwe munthu angapewele mayesero, m'mene angatengereko mbali posintha dela lake, umoyo wake ndinso popewa kusaweruza ena.

Maka-maka, ndife othokodza kwa Bambo Kelvin Bwalya, a Bambomkubwa a Amaritili a ku Uganda, kuja ku Luanshya, omwe anakonza njira zofalitsiramo uthengazi. Tithokodzanso Asemino a ku St Dominic's Major Seminary ku Lusaka, omwe anagwira nchito yotanthauzira.

Ngati mungafune uthenga wathuwu mwatsatane-tsatane, tilembeleni E-mail ku: jctr@jesuit.org.zm. Kapena mutha kuyang'ana mu kanema wathu wa zamaphunziro (website) potsatira izi: www.jctr.org.zm.

Tidzakhala okondwa kumva maganizo anu pa njira zofalitsiramo uthengazi .Maganizo anu adzatithandiza kukonza bwino zomwe tingadzalembe kutsogolo. Tikuthokodzani pa maganizo anu aphindu pa njira zofalitsiramo uthenga wa Adventi ndi wa Lenti za caka catha ca 2006.

Tikufunirani nyengo yabwino ya Lenti.

Zikomo, mtendere wa Ambuye!

Ndine,

Simson Mwale
Coordinator
JCTR Church's Social Teaching Project.

LAMULUNGU 1 MU LENTI - CHAKA C 25 FEBRUARY 2007

Mau Oyamba: Deteronomo 26:4-10
Mau Achiwiri: Aroma 10:8-13
Uthenga Wabwino: Luka 4:1-13

KUGONJETSA MAYETSERO

Talowanso mu nyengo ya Lenti, nyengo yodzadza ndi madalitso. Ino ndi nthawi yodziyang'ana ndi kuyambanso bwino kutsata njira za cikhristu mokhulupirika. Cibemba cikuti, "Iyapelelwa ilya ne cani", mau amene atanthauza kuti zinthu zikabvuta, munthu atha kucita ciliconse cimene cingamupulumutse. Panthawi ya mayesero obvuta cotereci, njira iliyonse yapafupi yopulumukira ingathe kugwiritsidwa nchito. Nthawi zambiri, anthu amene amapezeka m'mabvuto aakulu amasankha njira zoipa ndikukhulupilira zinthu zosayenera. Koma ngati akhristu, tiyenera kutsata Yesu amene pambuyo poyesedwa ndi Satana anagonjetsa mayesero (Lk 4:13). Tipeza malangizo abwino m'mwambi wa Citonga umene unena kuti: "kabayunge bakali bakawale", umene uticenjeza kuti tisamangotsata zilako-lako zathu. Kunena zoona, ngati munthu agonjetsa mayesero munjira iliyonse, wonyengayo amagonja ndi kungomusiya.

Lero ndi lamulungu loyamba mu Lenti. Nkhani imene tiwerenga mu Uthenga Wabwino wa Luka inena pa zoona zimene zilipo pakati pa zinthu zabwino ndi zinthu zoipa (Good and Evil). Yesu akumana ndi mayesero atatu, koma ndi mtima wonse, asankha zinthu zabwino ndipo agonjetsa Satana. Mulungu anatipatsa ufulu wakusankha umene nthawi zina timawuononga pa kusankha zinthu zosayenera. Anthu a dziko lililonse, mtundu uliwonse, mpingo uliwonse komanso munthu wina aliyense amakumana ndi mayesero. Mu umoyo wa masiku ano , pamene ambiri mwa anthu a mu Zambia ali m'mabvuto osaneneka, mayesero ofuna kucita zinthu zolakwika ngati njira imodzi yofuna kupezera umoyo wabwino ndiyo iwoneka ngati khalidwe. Ncifukwa cake zinthu zoipa monga ciwere-were, umbava wocita kuthyola nyumba, ciphuphu ndi zina zotere zapita patsogolo. Omwe samagwiritsa nchito "mpata" wopeza zinthu pakugwiritsa nchito njira zoipa amawoneka zitsiru komanso wopanda nzeru. Tiyeni pamodzi tisinkhe-sinkhe pamayesero atatu amene yesu anapitamo.

Yeso loyamba, Yesu ayesedwa kuti asandutse miyala kukhala mkate (Lk4:3). Yesu satsutsana nazo zoti munthu angadye mkate. Koma iye angofuna kutisonyeza colinga cake padziko cofuna kutithandiza kuti tileke kudalila cabe pa cuma komanso zinthu zathupi pa umoyo wathu. Angakhale anthu ena anena kuti "palibe ndalama palibe moyo", pali ndithu cinthu cina cabwino kuposa kupata cuma. Panthawi ino, pamene umoyo ndiwobvutirapo, kuwoneka kuti anthu akhudzidwa kwambiri ndi cuma, poganiza kuti ndiye muyeso wa umoyo wabwino. Ngati wina awona kuti umoyo wake ndi umoyo wa umphawi, amada nkhawa, asokonezeka komanso akhala wosakhutira.

Motero, zinthu zina zabwino monga ubale ndikupititsa patsogolo umoyo wabwino zimawonongeka. Tsono, atsogeleri a boma, anthu amalonda, ndi atsogoleri ena onse sayenera kugwiritsa nchito yankho ya Yesu loti 'Munthu sakhala ndi moyo podya mkate cabe' pofuna kuwononga moyo wa anthu awo mwadala. Atsogoleri sayenera kuwononga mwadala zinthu monga umoyo wa anyantchito, cisamaliro ca zaumoyo wa anthu, ndi umoyo wa zamaphunziro. Tiyenera kukhulupirira kuti cakudya cokha sicikwanira cifukwa Mulungu ali ndi njira zake zothandizira.

Mu yeso laciwiri, Yesu ayesedwa kuti agwiritse nchito mphamvu zake modzikonda. Nthawi zambiri, yeso limeneli limacitikadi mdziko lathu masiku ano. Pali malipoti ya anthu amene agwiritsa nchito njira ina iliyonse ncolinga coti akhale atsogoleri. Izi timaziona pa ndalama za nkhani-nkhani zimene anthu amagwiritsa nchito pakumemeza masankho (*campaign*). Ena amaba, kupereka anzawo (*betray*), ngakhale kupha komwe kuti akhale atsogoleri. Kuwonjezera apo, pali ena amene acedwetsera dala kapena kuwononga dala njira yakupangilamo malamulo atsopano a dziko ngati njirayo ingawasokonezere kudyelera maudindo awo. Pali kanthu kena mwa ife kamene kamatiuza kuti ulamuliro tiziugwiritsa nchito modzikonda osati pakuthandiza ena. Nkoyenera tsono, kuti aliyense amene ali ndi udindo adziyang'ane mwa iye yekha. Atsogoleri a zandale, a mipingo ndi ena onse

ayenera kudzifunsa funso ili : Kodi utsogoleri wanga uyenera kugwirira nchito anthu ena, kuonjezera mphamvu zanga, kapena kudzigwirira nchito ndekha?

Muyeso lotsiriza, Yesu afunsidwa kuti alumphe kuchokera pamwamba pa tempile ndipo auzidwa kuti anjelo adzamuchinjiriza (Lk. 4:9). Masiku ano, kuoneka kuti kuli lamulo losalembedwa limene linena kuti, “Chitani zozizwitsa ndipo anthu adzabwera kwa inu.” Ndikofunikira kwambiri kuti tiyang’aneponso moonadi pa kudzipereka kwathu mu uzimu. Nchifukwa nchiani ndifunika kukhala mu umoyo wachikhristu weni-weni? Kodi nchifukwa cha chikondi changa cheni-cheni cha Mulungu? Kodi ndimalankhula kuti ndine mkhristu wa khama ndipo Mulungu afunika kunisunga bwino? Kodi ndimatenga Mulungu ngati mbwezera chitetezo (*insurance policy*) ndipo kuti ayenera kundilipira tsopano chifukwa cha ubwino wanga? Chikondi choona cha Mulungu ndi chimene sichiika Mulungu mu mayesero kapena kumtenga ngati mbwezera citetezo.

Mu nthawi ino ya Lenti, tiyeni tidzionenso mu umoyo wathu potsatira citsanzo cha Yesu pakugonjetsa mayesero. Ngati umoyo wathu sulingana ndi umoyo wa Yesu, ndiye kuti tifunika kusintha mwamsanga. Tiyeni titsatire Yesu amene ngakhale kuti “anayesedwa mnjira zonse, sanachimwe.” (Heb 4:15). Popeza kuti tidziwa kuti “aliyense amene adzaitana dzina la Ambuye adzapulumuka” (Rom 10:13). Tsono tiyenera kumuitana iye ngati tifuna kuti tipambane pa kugonjetsa satana. Moposa zonse, Mulungu amene anapulumutsa Aisraeli kuchokera mu unyolo wa ukapolo ku Egipito, monga momwe tawerengera mu chowerenga choyamba, iye sadzatilekelera (Deut 26:8). Monga momwe tawerengera mu Uthenga Wabwino, satana adzagonjetsedwa ndipo adzatisiya (Lk 4:13).

MAFUNSO OTSINKHA-TSINKHAPO NDI KUGAWANA MUZIMBUMBA

- Kodi ndimazindikira ndi kukana mayesero amene ndikumana nawo mu umoyo wanga?
- Kodi ndimachita chiyani ndikakumana ndi mayesero atatu amene Yesu anakumana nao?
- Kodi tingachite chiyani ngati mbumba kuti tithandize anzathu kuti asagwere mu mayesero ndi uchimo?

TSEWERO

Mupeze mabanja awiri. Banja A ndi lotanganidwa ndi makhalidwe ake apamwamba. Banjali limaona mu zoulutsidwa mu mapepala, magazini ndinso mu mabuku akafukufuku (journals) pofuna ma fashoni atsopano, maphikidwe atsopano a zakudya, ma lamya atsopano (latest phones), zoimba-imba ndinso zocitika mu tauni. Mkupita kwa nthawi, cuma ciwathera ndipo akhala banja lacabe-cabe limene tsogolo lake silioneka bwino.

Banja B ndilokhutira ndi zimene liri nazo ndipo lilibe nthawi yolinganiza makhalidwe ake ndi mabanja ena. Banjali lidziwa zosowekera zake ndipo lithokodza Mulungu pa cuma cake. Mkupita kwa nthawi, banjali likhala lochita bwino ndipo linka nlitukuka ndipo likhala citsanzo ca banja lodzicepetsa ndiponso lochita bwino limene liika Mulungu patsogolo mu umoyo wake.

MAPEMPHERO A AKHRISTU

- Ambuye, tipempherera onse amene anagonjera mayesero chifukwa cha umphawi kuti abwerere kwa inu ndipo azindikire nchito za dzanja lanu mu zobvuta za umoyo wao. *Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze!*
- Ambuye, tipempha mphamvu zogonjetsera mayesero kuti tikutsatireni mokhulupirika. *Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze!*
- Ambuye, tipempherera onse amene ali ndi udindo wa utsogoleri kuti agwiritse nchito utsogoleri wao pothandiza anthu amene ali m’manja mwao. *Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze!*

LA MULUNGU 2 MU LENTI – CHAKA C 04 MARCH 2007

Mau Oyamba: Genesis 15: 5-12, 17-18
Mau Achiwiri: Afilipi 3:17-4: 1
Utenga Wabwino: Luka: 9: 28-36

KUITANIDWA KUTI TISINTHE UMOYO WA ANTHU

Ndi chinthu chodziwika bwino-bwino kuti munthu atagula katundu kapena atapedza chinthu china chatsopano, amakhala woteketseka ndi wokondwa pa nthawi yomweyo. Ambiri amafulumira kuyetsetsa kuti adziwe zabwino zones zomwe katundu wawo wabweretsa. Titsinkhe-tsinkhe za munthu yemwe wangogula galimoto latsopano, njinga, wayalesi kapena nyumba. kuteketseka kumakulilapo maka-maka pa nthawi yo khadzikitsa boma latsopano, malamulo atsopano (New Constitution) kapena ndondomeko ya za chuma (Budget). Anthu azakondwa ngati zinthu zatsopano ndi zabwino kopotsa zakale. Pa la mulungu la chiwiri mu lenti, ndife oitanindwa kutsinkha-tsinkha pa kusinthika kwa ambuye Yesu komwe kutiululira za ulemelero wake mtsogolo.

Mu mau oyamba alero ochokera mu buku la Genesis, tamva momwe mulungu anapangira phangano ndi Abraham, tate wathu muchikulupiriro. Mu mau achiwiri, Paulo woyera m'kalata kwa Afilipi, alufotokoza kuti kuphelezeleka kwa phanagano latsopano kuli mwa Yesu Christu. Mu uthenga wabwino, muli nkhani ya momwe Yesu anasinthikira alikupemphera kwa atate. Malembo onse atatu, atiululira za chithunzi choona cha Yesu Khristu. Koma mu umoyo wake wonse wa Yesu, anthu sadamumvetse. Tidamva mu uthenga wabwino pa la mulungu loyamba mu lenti kuti satana anali ndi chikaiko mwa Yesu, anati "ngati ndiwe mwana wamulungu" (Lk 4:3). Pakati pa anthu amene analikufuna-funa kudziwa za Yesu, Yesu asinthika ndi kuziulula ngati mwana wa mulungu (Lk 9:35). Kamanso kupezekapo kwa Mose ndi Eliya (Lk 9:33) kutanthauza kuti malamulo akale ndi zomwe aneneri ananena, zapherezeka mwa Yesu.

Kusinthika kwa Yesu tsiku la lero kuthetsa makaiko a anthu pa Yesu Khristu. Zomwe zichitikira ophunzira a Yesu, tizione ngati ziri kuchitikira ife lero. Mwachidule, kukumana kwathu ndi Khristu lero, kutithandize kumvetsa kweni-kweni kwa tsopano za Yesu Khristu. Mwa ichi, nthawi iriyonse pomwe tikumana ndi Khristi mu masakramenti pakhale kumvetsa ndi umoyo wa tsopano mwa iye. Nyengo ya lenti itipatsa mpata wotsinkha-tsinkha pa umoyo wathu ndi kuona ngati tirikusinthika.

Nthawi zones mu Zambiya timalaka-laka kuti mwina zinthu zinakakhalako mwa njira ina. Pafupi-fupi mbali zonse za umoyo wa anthu lero, zifunika kusinthika kuti umoyo wa anthu utukuke. Umoyo wathu wachikhristu usinthike. Pakhale akhristu achangu, achidwi, komanso okhulupiririka pakati pathu. Mafumu athu nawonso akhale okhulupiririka ndipo asachite za uphuphu ndi andale. Andale nawonso akhale okhulupiririka, ogwira nchito mwa mphamvu komanso osamalira zosowekera za anthu. Chonco, ndale za chiwembu kapena m'patuko zisaloledwe pakati pathu. Kutukula dziko ndi kuthetsa umphawi ndizo zinthu zofunikira. Sitingathe kukhala anthu opempha-pempha nthawi zonse. Mau ena mu Chiwemba akuti, "insala ni ndiminwa te mpulilwa iyo," kutanthauza kuti kuthetsa njara ndi kugwira nchito molimbika osati kumapempha-pempha. Ansenga nawonso amati, "mwana wachete olilira pansi," kutanthauza kuti mwana wamasiye sazakhala pansi ndi kumalira, koma azagwira nchito molimbika pa nthaka. Malamulo athu pa nthawi ino m'dziko lathu afunika kusinthidwa kuti akhale osamalira moona zosowekera kapena zofunikira za anthu mu ufulu wawo.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"*Promoting Faith and Justice*"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Web : www.jctr.org.zm

Izi zinthu zitha kusinthidwa kuti zikhale bwino ndi madalitso a Yesu Khristu. Tiwalole ambuye kuti asinthe umoyo wa anthu. Mu umoyo wawo, ambuye Yesu anathunzitsa ndi kusintha mitima yotsweka ya anthu, opwetekeka, akhungu ndi onse anali patali ndi mulungu. Ngati akhristu, tizindikire mu umoyo wanthu kufunikira kwake kwa kusinthika ndipo tithandizenso anthu onse ofuna thandizo lathu kuti asinthike. Pa nyengo ino ya Lenti tiyeni tichite zinthu zomwe ambiri amaona ngati sizingatheke konse. Mwa chitsanzo, kudya pamodzi ndi otilakhwira, kapena kupereka mpatso ya mtengo wapatali kwa osauka, kapena kutengapo ndi kusunga mwana m'modzi mwa ana opezeka mu mitseu (street kids). Tikatero, tizathandiza kusintha umoyo wathu ndi umoyo wa anthu omwe timakhala nawo. Chonco, ndi thandizo la Khristu, mathupi athu ofoka azasinthika ndi kukhala thupi la Khristu la ulemelero (Afilipi 3: 21).

KUTSINKHA-TSINKHA PA MAFUNSO MU ZIMBUMBA

- Kodi ndani pakati pathu amene afunika thandizo mwa msanga?
- Kodi ndi mbari ziti zotikhuza mu umoyo wathu zomwe zifunika kusinthidwa?
- Kodi tizachita chiani ife ngati banja limodzi chaka chino kuti tisinthe umoyo wathu kuti ukhale wabwino?

TSEWERO

Pakhale munthu mwamuna kapena mkazi woonda yemwe sazisamalira bwino ndipo amadwala nthawi ndi nthawi. Anthu ambiri safuna kukhala naye pafupi chifukwa ali ndi kabvumba koipa. Nthawi zonse ngati apita ndi njira, tiana timamulondola ndi kumamuitana maina oipa. Koma m'khristu wina wachifundo amuyendera ndi kumugulira zobvala, chakudya ndi kumulangiza pa za ukhondo pa umoyo wake. Anthu ambiri ndi odabwa pa kumuona ngati munthu wosinthika ndipo onse atsangalara.

MAPEMPHERO

- Ambuye, tikupemphani kuti mutipatse matso ndi makutu atsopano achikulupiriro kuti tithe kuchitapo kanthu ngati tiona ndi kumva kulira kwa otsauka pakati pathu. Ambuye mutimvere.
- -Tipempherere atsogoleri athu azandale, ampingo ndi mafumu athu kuti akhale nacho chidwi pa anthu awo m'mitima mwawo ndipo kuti akhale ozipereka pofuna kusintha umoyo wa anthu. Ambuye mutimvere.
- Tipempherere magulu onse osowekera pa za umoyo wawo, obvutika pakati pathu kuti mulungu awathandize ndi kuwapatsa zosowekera zawo. Ambuye mutimvere

LA MULUNGU 3 MU LENTI - CHAKA C 11 MARCH 2007

Mau Oyamba: Eskodo 3:1-8, 13-15
Mau Achiwiri: 1 Akorinto 10:1-6, 10-12
Uthenga Wabwino: Luka 13:1-9

KUSINTHA MUDZI KUPYOLELA MUKAKHALIDWE KA MUTHU

Ngati zinthu sizili momwe tiziyembekezela kukhalila, zochita za anthu kaya kapena zinthu zomwe athu amachita zikhala zosiyanasiyana. Kungakhale ku malo antchito, ngati chisanzo, timamva kuti anthu alekeza kusewenza chifukwa salikuwalipira bwino, kaya kapena sali kusewenzela mu malo abwino, kaya mwina sawalipira panthawi yake malipiro awo apamwezi; izi zimachitika ndi anthu aja amene agwila ntchito mboma. Timaonanso izi ndi ana amaphunziro, amu masukulu akulu-akulu (college or university) amene amakana kulowa mukilasi kuti aphunzire ndipo amapanga chiwerewere kuti aonetse kusakondwa kwao ndizomwe zilikuchitika. Talandiranso mauthenga osiyanasiyana kuchokera ku anthu mu mudzi mwathu amene aonetse kusakondwa ndi kapanigidwe ka malamulo a dziko lathu. Kusakondwa kapena kudandaula kwaonetsewanso ndi akulu a ndale omwe sanakhoze mumasankho yapitaya ndipo anapeleka madandaulo awo kubwalo yamilandu kuti masankho siyanayende mchoona, panali kusakhulupiririka. Zonse izi ndizisanzo za momwe athu amaonetsera kusakondwa kwao ndi zinthu zomwe amachita kuti aonetse kuti pali zinthu zina zomwe zifunika kusinthika.

Pa sondo ino la chitatu mu Lenti, tiyeni tiyese kusinkhasinkha pakufunika kolapa kuti tipeleke umoyo wathu wachikristu pasogolo. Panthawi ino ya Lenti, tifunika kuona mu umoyo wathu ndikuyesa kusintha kupyolela mukulapa. Mu mau athu ya lero tikuona pakufinika kolapa. Kulapa ndikuzindikira kusakhulupirika kwathu mu umoyo wathu ndikukhala okonzeka kukonza momwe tilephera. Paja a Chewa amati, pepani sapoletsa chilonda. Ndiye kuti kufulumira kwa kulapa kwathu sikufunika kutipanga athu a mawu a pakamwa chabe koma kuti tionetse kulapa kwathu muzochita zathu. Ngati tikhala anthu a mua a pakamwa chabe, tingalinganizidwe ndi muthu amene alapa kuba lamya koma Sali okonzeka kubweza lamya ija kwa mwini wake. Kulapa kwathu kugwirizane ndi kusintha kwa mkhalidwe wathu.

Mu mau athu oyamba alero a mbuku la Eskodo tiona umoyo wokoma womwe Mose anakumana nawo. Mose anali wokonzeka kuti asinthe pomwe anakuma ndi mulungu mu chisamba choyaka moto chija. Mose anali ndi njira yake yake yaumoyo, ndipo analinso ndi maganizo yake yake pochita zinthu. Koma sanawayewaye pomwe mulungu anamuitana. Mulungu awalonjeza kuti aona kuvutika kwa anthu ake ndipo kuti ali okonzeka kuwathandiza. Mulungu anaululira Mose ndipo aululira ifenso lero kuti ndi Mulungu wosamala ndi wokonda anthu ake.Mu umoyo wathu naifenso timakumana ndi zinthu zomwe zimatiyembekeza ife kuti tisinthe mtima ndi makhalidwe. Zisamba zamoto zathu anga khale anthu osauka amene afunika thandizo lathu, anthu odwala ndiponso anthu amene alimdende amene afunika kuwayendera. A Bemba amati “Nangombe pabana taya”, kuthanthauza kuti Ngombe sithawa ana ake. Ndiye momwe mulungu amasamalila ana ake, maka maka iwo amene amazindikira kufunika kotembenuka.

Nchimodzimodzi naifenso, Mulungu aonanso kusauka kwathu mdziko lathu lino la Zambia. Mwachisanzo, kusowa kwa ntchito, kusasamala antchito kwa anthu amene achokera kumaiko akunja, madzi ndi mphepo akuipisiwa, matenda ya kalionde-onde (HIV-AIDS), kuchedwetsewa ndi kuchepa kwa ndalama za pa mwezi za anthu osewenzela mboma, izi ndi zina ndiwo mabvuto yomwe timakumana nawo, Mulungu amva kulira kwa ovutika mudziko lino lathu la Zambia omwe mowelengeka afika 70% kufika 80% mwa anthu onse amdziko lathu lino. Chiyembekezo chathu chilli mwa Mulungu wa chikondi omwe anapulumutsa anthu aisraele kuzingwe zawo. Zingwe zomwe tifunika kuchosewamo ndi chimo. Tingakwanilitse zimenezi ngati tili okonzeka kuyankha kuitanidwa kwathu koti titembenuke. Tifunika kukhala anthu ofuna kusintha kuti tikwaniritse kusintha Mudzi momwe tikhala.

Uthenga wabwino walero utionetsa zakukula kwa ntchito yolapa pomwe timva kuti mukapanda kutembenuka kapena kulapa nainunso mudzaonongedwa ngati iwo aja (Luka 13:5). Fanizo la mtengo wamkuyu ulinganiza chimo ndi kusabala kwa mtengo wamkuyu. Chimo mu fanizoyi ilinganizidwa ndi

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"*Promoting Faith and Justice*"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Web : www.jctr.org.zm

kusabala zipaso kwathu kapena kulephera kwathu kuti tikhala anthu amene timafunika kukhala. Ngati akristu timasauka ndi kusabala zipaso kwathu. Kulapa mjira iyi kuthanthauza kusiya kumbuyo zonse zimene zitilepheretsa kukhala athu amene timafunika kukhala.

Mulungu atiitana kuti tichoke muukapolo wa chimo ndikukhala ndi ufulu womwe Mose anali nawo. Nchofunika kuti tiyetse kuyaangana mumalo momwe timakhala osafikapo ndiwosabeleka zipatso. Kambiri timaopa kuchita zofunika, timakhala anthu akaduka ndipo timakana kukhulukira anzathu. Zonsezi zimaumba momwe timazionera ife tomwe ndianzathu. Tonsefe, msinkhu ulionse, tikhale amuno mdziko kapena akunja, ukhale mtundu wosiyana, kaya ndise anthu okuda kapena achiyera, kaya tikhale ndi usogoleri mudzi, tonsefe timakumana ndichiyeso chofuna kuchimwa. Koma kuti tikhale ndi mkhalidwe wovomerezedwa pakati pa anthu tifunika kugwirizana ndi kuzipereka kuti tizisinthe ndi kusintha mudzi momwe tikhala.

Ngakhale tifunika kulapa mwamsanga, tifunika kudziwa kuti kutembenuka kutenga nthawi. Kutembenuka sikuchitika msanga monga momwe munthu amasegulila maso kaya kapena kuyatsa nyale.Munthu aliyense amene afuna kulapa afunika kukhala ndi mtima wofuna kuzilanga chifukwa cha machimo yomwe anachita. Lomba kodi tingaonetse bwanji zimenezi? Nchofunika kukhala ndi malingalilo ya umoyo wathu wonse. Mwachisanzo, ngati ndiwe mkulu wa ndale wosakhulupirika ndipo wamtima wonzunza anzako ufunika kusintha. Chimodzimodzi, ngati ndiwe mayi kapena bambo wosakhulupirika mbanja, mwana wamkhalidwe woipa kapena mkristu wachi mayi kapena bambo wozikonda, tonsefe tifunika kusintha kuti tikhale anthu abwino. Sitifunika zinthu zozwizwitsa kaya kapena kuyembekeza kubwera kwachiwiri kwa Yesu kuti tisinthe. Ino nthawi ya Lenti litipatsa mpata kapena nthawi yoti tilape mofulumira ndi kutembenuka.

Kulapa kutipempha kuti tikhale woona ndi ife tokha kapena ndi umoyo wathu ndikuvomera kusabeleka zipaso kwathu. Tikasinkhasinkha motere ndiye pomwe tizakhala ndi ululu wa zinthu zomwe timalephela kuchita. Ululu uyu uzatithandiza kuti tikhale anthu ozichepetsa ndikuzipeleka kwa kristu kuti atichotse muzingwe za chimo ndikutipatsa mtendere. Tsono tiyeni tione kuti nthawi ino ya lenti ikhale nthawi yozikonzekela kuti tilape ndikutembenuka mjira zosiyanasiyana. Tiyeni tigwiritse ntchito sacramenti ya chilapiro.

MAFUNSO YOTSINKHA-TSINKHAPO NDI KUGAWANA MUZIMBUMBA

- Kodi ndimaona kufunika kwa kulapa ndi kupempha chikhulukiro kwa Mulungu ndi anzanga omwe ndikhala nawo?
- Ndimbali zotani mu mbumba yathu zomwe zifunika kusithiwa mwamsanga?
- Kodi tilikuchitapo chiani kapena tilikundandamika zinthu zotani zomwe zifunika kusinthika mziko lathu?

TSOWERO

Pali banja lina lomwe ili mumavuto chifukwa chokhuta mowa kwa mmodzi mwa makolo. Wamkazi kapena wamuna kapena ana kapena onse anthu ali pafupi salikukhala mumtendere chifukwa cha khalidwe imeneyi la bambo kapena mayi uyu. Koma pamene mayi uyu kapene bambo uyu apulumuka mgozi aliokhuta mowa, munthuyu asankhula kuleka kumwa mowa. Banja ndi onse okhala pafupi akhalanso ndi mtendere ndipo amulimbitsa mayi kapena bambo uja kuti asakamwenso mowa. Chikondwelelo chibwereranso mbanja ndi mudzi ndipo munthu oleka kumwa uja akhala wathanzi ndipo asangalala ndi mkhalidwe watsopano womwe uli wa mtendere ndi wa ulemerero.

MAPEMPHERO YA AKRISTU

- Ambuye, tipempherera atsogoleri a mpingo kuti apeleke chisanzo chabwino cha umoyo wao. Ambuye mutimvere; Tikupemphani mutivomereze.
- Ambuye, tizipempherera ise tomwe kuti tiziwe kufunika kwa kutembenuka, kulandira chilapiro ndi kukhala anthu okonda ndi osamalila anzao. Ambuye mutimvere, Tikupemphani mutivomereze.
- Ambuye, tipempherera onse anthu amene sakuziwani ndi onse amene anatayika kuti azindikire chikondi chanu paiwo. Ambuye mutimvera; Tikupemphani mutivomereze.

LA MULUNGU 4 MU LENTI – CHAKA C 18 MARCH 2007

Mau Oyamba: Joshua 5:9, 10-12
Mau Achiwiri: 2 Akorinto: 5:17-21
Uthenga Wabwino: Luka: 15:1-3, 11-32

KHALANI OMASUKA KUKHULULUKIRANA NDI KUYANJA

Nthano yamwana wosowa ndi tate wokhululuka yomwe timawerenga mu uthenga wabwino ndi nkhani yodziwika kwambiri. Nthanoyi yakhala ikufotokozedwa nthawi zambiri maka-maka pakulankhula za chikhulupiriro ndi chiyanjano. Zomwe anachita atate a mwanayu, kwa ena ndi zinthu zosamveka maka-maka kwa iwo omwe amafuna kubwezera choipa ndi choipa (revenge). Koma chimwemwe cha mwana wokhululukidwa sichingathe kubisika. Ngati akhristu, tikhale okonzeka kukhululukirana ndi kuyanjana. Paja mu Chichewa timati, "Choipa citsata mwini", kutanthaudza kuti wochita choipa, malipiro ake ndi mabvuto.

Mu mau oyamba alero, mu buku la Joshua, tamva momwe Aisraeli anafikira kuchokera ku Egipito. Joshua akuti, "Lero ndamuchotserani manyazi aku Egipito (Joshua 5:9), kukhala ngati mau ofotokoza za ufulu wa Aisraeli. Paulo woyera mu kalata wake kwa Akorinto mu mau achiwiri, atsimikiza za kubwera kwa chiwiri kwa Khristu kuzayanjanitsa dziko lapansi. Ili ndi nchito la Mulungu, choncho ife tonse tiyanjane naye Mulungu. Nthano ya mwana wosowa mu uthenga wabwino ifotokoza mwa chidule mfundo zones zomwe ziri mu mau athu alero.

Pomwe tili pafupi ndi chikondwerero cha Pasaka, ndi chofunikira kwabasi kwa ife akhristu kulandira sakramenti la chilapiro. Mwana wosowa uja anazindikira kuti zinthu sizinamuyendere bwino ndipo anaganiza zoti abwerere ku nyumba. Zinthu zinam'khalira bwino atatero. Tiphunzire nafenso kukumana ndi choona, tichite manyazi ndi machimo athu ndipo tilape. Tizindikire kuti ngakhale achuluke ndi kukula bwanji machimo, Mulungu ndi wokonzeka kutilandira ndi chimwemwe.

Pofuna kufotokoza za kukoma kwa Mulungu atate athu, ifenso tipereke uthenga wa chikhululukiro kwa makolo ndi otisamalira mu manyumba mwathu. Ngati mwana wamkazi mwina wapezeka ndi pakati, kapena mwana wa mwamuna ndi chidakwa kapena wotsuta chamba, makolo akhale nawo mtima wokonzeka kubvomera mwana wawo wopempha chukhululukiro. Chikondi cha makolo pa ana awo, chifane-fane ndi chikondi cha Mulungu pa ana ake.

Monga mau ena mu Chiwemba amati, "Umwana kasembe, kakukoma wakoweka", kutanthauza kuti mwana ali ngati nkhwangwa, yomwe ngakhale yakupweteka, umaitsenza ndithu pa mapewa chifukwa ndi chipangizo chofunukira. Komanso mu Chichewa timati, "Chibale ndi listiro, sichisansika", kutanthauza kuti banja liri ngati tsiro pa thupi lomwe sitingathe kuchotsa. Umodzi mu mabanja pa mabvuto kapena pa chikondwerero ndi chinthu chofunikira.

Kufunikira kwa kukhululukirana kumatipempha ife kuti tizichepetse ndipo tokonde anzathu ndi kuyanjana. Pamene pali chiwembu palibe umoyo wabwino. Pa umoyo wathu, timafuna anzathu kuti tikhale bwino ndi kukula.

Chimodzi-modzinso, atsogoleri amuzimbumba kapena mabungwe ndi mipingo akhale okonzeka kukhululukira onse otayika. Ngati m'modzi wa akhristu watayika, ndi udindo wa

m'khristu aliyense kum'thandiza kuti abwerere mu umoyo wa chkhristu. Kunyodola kapena kunyoza m'khristu wotayika sikuthandiza ayi. Tiri nazo zitsanzo zochuluka za azimuna omwe amathawa mabanja awo atalandira ndalama za malipiro a nchito zawo, amakwatira azikazi ena, koma ngati ndalama zatha, amabwereranso ku mabanja awo. Nanga udindo wa m'khristu ngati zintu ziri tero ndi chiani? Kodi ndikumaseka chabe? Ayi, pali chinthu chomwe tingathe kuchitapo. Mwa chitsanzo, kuthandiza ndi kuthunzitsa mabanja okhumudwa.

Nthano ya mwana wosowa ilinso ndi punzitso kwa iwo woyang'anira amundende. Umoyo wa amundende siuli bwino, anthu afunika kuchitapo chimodzi. Oyang'anira anthuwa, afunika kuzindikira kuti nchito yawo ndiyothandiza amundende kusintha. Amundende safunika kunyozedwa kapena kupandidwa, koma amafunika kuwaonetsa chikondi pakuwasamalira bwino. Komanso, ngati amatsulidwa, anthu awalonjere bwino. Kuwapondereza kapena kuwanyodola sikuthandiza ayi.

Atsogoleri azandale nawonso atengepo phunziro pa tate wokhululuka mu nthano kuti nawonso akhale nawo mtima wokhululuka ndi kuyanjana maka-maka ndi andale anzao. Izi ziri tero chifukwa akhristu afunika kukhala ndi chidwi chokhululukirana nthawi zones. Paja awemba amati, "Umusuku ubi, ubifya impanga", kutanthauza kuti mkuyu woipa umaipitsa nkhalango. Choncho ngati akhristu saonetsa chitsanzo chabwino pa kuyanjana ndi anzao, ndiko kuti titha kunena kuti onse akhristu sakhululukirana. Choncho, pali ponse pomwe pali akhristu, awale ngati nyale ndipo mwachimwemwe akahle okhululukirana ndi oyanjana.

KUTSINKHA-TSINKHA PA MAFUNSO MU ZIMBUMBA

- Kodi ndine wokonzeka kukhululukira ndi kuyanjana nawo onse ondilakhwira?
- Kodi ndichitapo chiani kuti ndithandize omangidwa mu ndende?
- Kodi tichitepo chiyani ngati mumba kuti tithandize mabanja omwe azimuna kapena azikazi awo anawathawa chifukwa cha m'modzi kukhala ndi matenda akalionde-onde (HIV/AIDS)?

TSEWERO

Pekani banja lomwe likhala bwino ndi chimwemwe mu umoyo wawo. Mwana m'modzi mwadzidzidzi anaganiza zochokapo pa nyumaba, mwina chifukwa cha m'khalidwe wake woipa. Patapita miyezi mwana uja anazindikira kulakhwa kwake ndipo anaganiza zoti abwerere ku nyumba. Mwana uja anamulonjera bwino kunyumaba ndipo anayambanso kukhala bwino.

MAPEMPHERO

- Ambuye, tikupemphani kuti mutipatse nzeru zofuna kukhala amodzi mu mabanja ndi muzimbumba mwathu. Ambuye mutimvere.
- Ambuye, tipempherera onse obvutika ndi matenda a Kalionde-onde (HIV/AIDS) kuti muwathunzitse mitima, ndipo mutiphunzitse nafenso kuwathunzitsa mitima. Ambuye mutimvere
- Ambuye, tikupemphani kuti mutipatse mzimu wanu, utitsogolere pa nthawi ino ya Lenti kuti tikasangalale pa Pasaka. Ambuye mutimvere.

LAMULUNGU 5 MU LENTI - CHAKA C 25 MARCH 2007

Cowerenga Coyamba: Yesaya 43:16-21
Cowerenga Caciwiri: Afilipi 3:8-14
Mthenga Wabwino: Yohane 8:1-11

MUSADZUDZULE

Tamva maripoti ambiri-mbiri a anthu omenyedwa kapena kuochedwa ncholinga cofuna kuwapha pambuyo powagwira akufuna kucita za umbava. Mmaiko ena, tikumvanso za kutemedwa miyala kwa anthu amene agwidwa akucita cigololo. Anzathu ambiri amafulumira kuweruza ndi kudzudzula. Kawiri-kawiri, anthu amene sanagwidwepo amapeza mpata wodzudzula anzao. Kenaka amakonda kugwiritsa nchito miyambi, monga uyu wa ciBemba woti "Changa baseka uwacelwa" (yemwe wagwidwa ndiye asekedwa koposa) kapena wa Citumbuka woti, "Uheni ngwa banyabo" (nthawi zonse wolakwa ndi ena). Nthawi zambiri timakhala ofulumira kuona zolakwa mwa anthu ena ndi kufunitsitsa kuti mpaka atalangidwa.

Koma timafunika kuona pa zimene tinali kufunika kucita, zomwe sitinazicite, ndipo zapangitsa zinthu kuti ziyende molakwika. Mwacitsanzo, kuphunzitsa mwambo wacikhristu ku ana athu, kukhala okhulupilirika m'mabanja. Tisamaonetsa kulakwa kwa anzathu pamene ife sititha kucitapo kanthu kena kalikonse, koma kumaweruzana mwa cikondi ngati abale ndi alongo.

Tsiku la lero, ndi lamulungu la cisanu mu Lenti, kotero kuti posacedwapa tidzacita cisangalaro ca kusauka, kufa ndi kuuka kwa ambuye athu Yesu Khristu. Masiku makumi anai acikonzekero ali pafupi kutha, nthawi yoyeneradi imene ife akhristu tiyenera kudzifufuza m'makhalidwe athu ndi kusintha pa kulapa za kwaipa zathu zonse.

Mcowerenga coyamba ca lero, mprofeti Yesaya ali kutiuza za cikondi ca Mulungu amene atha kupanga njira ngakhale pa nyanja. Ici ndi cisonyezo conena kuti, kulibe cinthu cina ciliconse cimene cingathe kusiyanitsa cikondi ca Mulungu pa ife. Mulungu atha kupanga zinthu mwatsopano malinga tatembenuka, ndi kuleka kuganiza macitidwe athu akale monga momwe mwambi wa Cibemba uticenjezera kuti: "Akabwelelo kalalya" kusonyeza bvuto lokhalilira mu makhalidwe akale. Uku nkuitanidwa kwa anthu ocita zoipa kuti ayesetse kukometsa umoyo wao. Mwacitsanzo, mbala zileke kuba, acigololo aleke kukhala wosakhulupililika, ndiponso abodza aleke kunena zonama.

Mu Yesaya 43:19, Ambuye akunena kuti adzacita zinthu zatsopano. Ncifukwa cace m'masiku womaliza ano acikonzekelo ca caka ca cisangalalo ca kuuka kwa ambuye Yesu, tiyeni tidzimasule mwaufulu wathu popanga zinthu mwatsopano, pakulapa mcoonadi. Ndife anthu ake amene anadzipangira iye mwini kotero kuti sangatilekelere kapena kutidzudzula. Koma amaonetsabe cisamaliro cace pakuti aitana ife ku cikondi ndi cibwenzi cace kupyolera mu sacramenti ya kulapa.

Ndife anthu osiyana-siyana m'makhalidwe ndi m'macitidwe athu. Ena ali ngati wophunzira uja, Yohane, pakuphunzira ndi kulapa mwamsanga, ndipo pakutero akhala ndi cikondwerero cifukwa cogwirizana naye Mulungu. Ndipo ena ali ngati wophunzira Petro, amene anabvomera kuweruzidwa kawiri-kawiri ndi kuphunzira zinthu mnjira yosautsa. Cinthu cimodzi cimene tiyenera kudziwa ndi cakuti Mulungu sadzatilekelera kapena kutikhalitsa aciwiri ku cinthu cina ciliconse mu umoyo wathu, koma adzasewenzetsabe njira zosiyana-siyana ndi mphamvu za Mzimu Woyera pokhazikitsa cikhalidwe cacikhristu mwa ife. Tifunika kukhala anthu odzipeleka ku maphunzitso a Mzimu Woyera mwa ife.

Mu Uthenga Wabwino wa Yohane wa tsiku lalero, tikumana ndi mzimai wogwidwa akucita cigololo. Codabwitsa ndi cakuti, mwamuna sanachulidwe ai. Ici ndicitsanzo ca mpatulo pakati pa amuna ndi akazi. Izi zimacitikanso m'mizinda yathu, pamene akazi amapatulidwa, mwa citsanzo, popanga malamulo. Molinganiza ndi izi, tili nawo amuna ambiri wophunzira amene ali kusangalala m'maudindo aulemelero. Cokhumudwitsa ncakuti akazi ambiri akhala ngati zida zokondweletselako mathupi a amuna mwa njira za ciwerewere; mwacitsanzo masiku akumbuyoku, akazi amagulitsidwa ku maiko akunja kucokera mdziko lathu la Zambia ndi m'maiko ena a mu Africa. Tiyenera kuzindikira kuti akazi

atengako mbali yofunikira m'mizinda yathu kotero kuti nkofunikira kuwateteza ku njira zonse za mpatulo ndi zoononga ufulu wao. Kumbukirani kuti, mukaphunzitsa mtsikana, ndiko kuti mwaphunzitsa dziko.

Yankho la Yesu kwa wonenezera, ndi umboni wa ulemu umene iye anali nawo za ufulu wa cibadwidwe. Atizindikilitsa kuti tiyenera kuganizira pa kufoka kwathu poyamba tikalibe kuganizira kulakwa kwa anzathu. Mwambi wa ciphunzitso cacikulu ndi uyu: "Ukaona munthu wocita zolungama thokodza Mulungu, ndipo ukaona wocimwa, ndziyang'ane iwe wekha." Mcoonadi tiyenera kuyesetsa kupewa kuloza zala anzathu mzolakwa zao pamene ife tomwe tikalibe kudziyang'ana mzolakwa zathu.

M'mizinda yathu masiku ano tiona anthu andale ambiri omwe amacita zinthu mokondera ndikufulumira kuona zoipa za anzao ndipo amakhala cete ngati adani ao acita zinthu zabwino. Ndiye tonsefe timadziwa bwino lomwe kuti citukuko ceni-ceni cingakwaniritsidwe kupyolera m'cigwirizano osati udani, kapena mpatulo.

Yesu aonetseratu poyera kuti ngakhale ndife ocimwa koposa, satiweruza iye mwini. Koma kutenga njira zathu, kucita zinthu zokomera ife citanthauza kukana ulamuliro wa Mulungu ndi kuzionongera tokha umoyo wathu. Mulungu safuna ife kukhala anthu ofufumuka, osangalala mu umoyo wathu koma osakumbukira anzathu. Sitingathe kupewa za cikunja m'mizinda momwe tikhala koma tingathe kupewa zinyengo za akunja momwe Yesu anacitira. Monga momwe mau ena anena, "Sitingaletse mbalame kutera pa mitu yathu koma tingaziletse kupanga zitsa mu tsitsi lathu." Mu caka cino ca Lenti, tiyeni tipange maganizo yathu kuti abvomere zomwe Mulungu afuna. Tikatenga cikalata cacilolezo cophunzira kuyendetsa galimoto, timayesetsa kusunga malamulo ya pamseu. Sitimaganizira konse kuti tsiku lina tidzagwiritsa nchito mbali yomwe sitiloledwa kugwiritsa nchito. Momwemonso, ngakhale kuti tatembenuka mtima, tiyeni tisunge maganizo athu oyera pakupewa zonse zimene zingatiipitse ndipo timvetsere ku mau a Yesu omwe adzatisunga. Mnjira imeneyi, tizakwanilitsa kukhala ndi maganizo a Khristu.

Tiyeninso tigwiritse nchito mau athu, yolankhulidwa ndi yolembedwa, kuthandiza, kulimbitsa ndi kukulitsa akhristu anzathu ndi kuthandiza akunja kumvetsa za ufumu wa Mulungu. Tiyeni tiwaonetse cigwirizano comwe Mulungu afuna kukhala naco ndi iwo, cosawadzudzula koma cowasamalira. Tiyeni tiyesetse mu caka cino kulandira ocimwa monga momwe Yesu anacitira ndi kuwathandiza mnjira zonse kutembenuka mtima, kuti akhale odzipereka mu umoyo wa cikhristu.

MAFUNSO OTSINKHA-TSINKHAPO NDI KUGAWANA MUZIMBUMBA

- Kodi ndikucitapo ciyani kuthandiza anzanga kudziwa Yesu m'banja langa, ndi momwe ndikhala?
- Ndi mnjira zotani momwe akazi amapatulidwa masiku ano, mwa citsanzo pamwambo, mumasukulu, pa nchito, mnyumba ya Aphungu a malamulo (Parliament)?
- Ndi ciyani comwe tikucitapo ngati mbumba kuthandiza akazi omwe amanzunzidwa?

TSOWERO

Khalani ndi anthu awiri omwe acita colakwa cifanana. M'modzi amasulidwa ndipo wina acititsidwa manyazi ndi kunzunzidwa ndi unyinji wa anthu. Anthu onse amuseka. Ndipo mwana wamng'ono aimilira kutsogolo kwa wodzudzulidwayo, afunsa anthu onse komwe wapita olakwa uja wina. Mmodzi-mmodzi, onse anthu aja acoka ndi manyazi.

MAPEMPHERO A AKHRISTU.

- Ambuye, tipempherera akazi omwe kwa kanthawi akhala ali kunzuzidwa ndi anzao kuti abwezeredwe ulemelero wao. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutimvere.
- Ambuye, tikupempha kuti onse ali mu maudindo a ulamuliro kuti akumbukire akazi ndipo awakweze naonso pa malo a ulamuliro. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutimvere.
- Ambuye, tikupempherera anthu omwe anamizira anzao kuti aleke khalidwe lofuna kupeza choipa mwa anzao koma aike maganizo ao pa kukonza umoyo wao. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutimvere.